**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI


## KUYAMBIRA PA 03 MARCH MPAKA PA 09 MARCH 2025

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

M'sabatayi**, madera ena apitilira kulandira mvula, yomwe ikuyembekezeka kugwa makamaka m'madera am'mphepete mwa nyanja ya Malawi ndi ena am'zigawo za kumpoto komanso pakati** kamba ka dera lodzetsa mvula la I.T.C.Z (Inter-Tropical Convergence Zone). Palinso kuthekera kwakukulu kwa Namondwe kubadwa m'nyanja ya m'chere ya India pakati pa mayiko a Madagascar ndi Mozambique (Mozambique Channel) pofika Loweruka lino pa 08 March, 2025.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'madera ena kunagwa mvula, yomwe inagwa yamphamvu makamaka m'madera am'chigawo cha kum'mwera. Madera ambiri am'chigawo cha kumpoto ndi pakati sanalandire mvula. Mapu ali m'musimu akuonetsa ena mwa madera omwe analandira mvula msabata yangothayi.




*Mapu: Kagwedwe ka mvula kuyambira pa 23 February mpaka pa 28 February 2025*

## MALANGIZO MSABAYI

- **Madzi osefukira mwadzidzidzi:** Tikhale atcheru ndipo tipewe kuoloka madzi osefukira kapena othamanga kuti titeteze miyoyo yathu.
- **Mvula ya Mabingu:** Tikulangizidwa kubisala pamalo otetezeka bwino komanso tipewe kubisala pansi pa mitengo pamene mvula ya mabingu ikugwa.
- **Chinyezi:** Tikhale osamala ndi **nyumba kapena zimbuzi** zomwe zanyowa kale kwambiri ndi mvula chifukwa zitha kugwa nthawi ina iliyonse.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:***


*The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*



**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 02 March, 2025**